# SONGANI ZONE

## 2024 SONGANI ZONE STD 8 MOCK EXAMINATIONS

## CHICHEWA

**(100 MARKS)**

**Dzina la ophunzira:** ______________________________________________
(Yambani la bambo)

**Dzina la sukulu:** ______________________________________________

**Malangizo**

- Lembani dzina lanu komanso dzina la sukulu yanu
- Yankhani mafunso mosamalitsa
- Siyani kulemba komanso Perekani pepala lanu kwa oyang'anira mayeso mukafunsidwa kutero.

**GAWO A**

Yankahani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri omwe ali m'musiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata.

Mawu achimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 komanso asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu moto olusa. Mwazina tsatani izi polemba.

**Ndime yoyamba**

- Tsiku ndi nthawi yomwe moto udabuka.
- Chomwe chidayambitsa moto.
- Malo omwe kudabuka moto.

**Ndime yachiwiri**

- Dera lomwe motowu udawononga.
- Zinthu zomwe zidawonongeka ndi motowu.

**Ndime yachitatu.**

- Gawo lomwe mudatenga patsikuli.
- Thandizo lomwe likufunika mwansanga.

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa mkulu owona zamaphunziro m'dera lanu yomufotokozera za mavuto omwe mukukumana nawo pa sukulu yanu. Mwazina tsatani izi polemba.

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata
- Dzina la sukulu yanu
- Chiwerengero cha ana pasukulupo

**Ndime yachiwiri**

- Mavuto omwe mukukumana nawo.
- Zomwe mukufuna atakuthandizani mwansanga

**Ndime yachitatu**

- Chisangalalo chanu mukadzalandira thandizolo.
- Momwe muzadsamalire katunduyo.

**GAWO B. (20 MALIKSI)**

3. Werengani nkahni yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawo.

Pabwalo pamakhala kanenedwe kake ka milandu kamene kamatchedwa chowa. Chowachi chimachitika pofuna kuona bwino magwelo ake a milandu. Popeza kalero padalibe mchitidwe omalemba pamene oyankhula ali kufotokoza. Oweluza adali kubwerezanso mawu aja amene munthu wanena. Tsopano uja ofotokoza amabuula kuti mmm! mmm! Kuvomereza kuti obwereza mawu uja adali kulongosola molondola.

Pabwalo loweluzira milandu lotchedwa nkhani zathera pano, m'mawa tsiku loweluka dzuwa litangotuluka pang'ono, anthu adali kudikira amfumu bwana Lumbe kuti ayambe kuweluza milandu. Mwadzidzidzi anthu adaona mfumuyi ndi akulu abwalo, a Gudeya ndi a Muholo akutulukira kuti balamanthu. Anthu onse adangoti gwadu gwadu. M'menemo nkuti Mbumulire pamtima pake pali thi thi thi. Mfumu bwana Lumbe adali ndi chikaliwo wake chili ndi utsi kuti phwa, phwa phwa matsinya ali khwe, khwe, khwe ngati ayambana ndi munthu.

Ehe! Adayankhula mfumu bwana Lumbe akukhala pa chitsa cha mtengo. Nthawiyo akulu abwalo nkuti atakhala kale pansi . "Chete!" adatero nkulu wa bwalo la nkhani zathera pano. Tsono mverani mfumu bwana Lumbe "pano monga mudziwa," adatero mfumu bwana Lumbe "ndi pankhani zathera pano pamene mboni zikupereka umboni sindikufuna kumadzidula mawu. Pamene wina ali kufotokoza nkhani m'mene idayendera musamaikire mang'ombe. Pomaliza nkhani iliyonse ndizagamula molingana ndi umboni ndi kakhalidwe ka nkhani.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere iri pansi pa funso lililonse.

a. Kodi chowa ndi chiyani?

______________________________(Maliksi 1)

b. Kodi cholinga chochitira chowa ndi chiyani?

______________________________

______________________________(Malikisi 2)

c. Chifukwa chiyani oweluza milandu akale adali kubwerezanso zomwe anthu anena

______________________________

______________________________(2 Malikisi)

d. Fotokozani chifukwa chomwe ofotokoza milandu amabuulira.

______________________________

______________________________(2 Maliksi)

e. Perekani matanthauzo a mawu awa kuchokera m'nkhaniyi.

(i). Balamanthu

______________________________(2 Malikisi)

(ii). Mang'ombe

______________________________(2 Malikisi)

f. Kodi mawu oti akulu abwalo akutanthauzanji?

______________________________

______________________________(2 Malikisi)

g. Perekani mivekero iwiri kuchokera mu nkhaniyi

______________________________(2 malikisi)

h. Perekani dzina la mfumu ikupezeka m'nkhaniyi.

______________________________(2 Malikisi)

i. Perekani malo omwe nkhaniyi idachitikira.

______________________________(1 Malikisi)

j. Perekani mutu wa nkhaniyi.

______________________________

______________________________(2 Maliksi)

**GAWO C.**

4.Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

"Ine maliro oterewa sindingaikitse.
Malemu agona apawa anadula phazi kale
kumudzi kuno".

**Mafunso**

a. (i). Ndimalonje anji amenewa?
____________________________________________(1 Maliksi)
(ii). Angalankhule malonjewa ndani?
____________________________________________(1 Malikisi)
(iii). Mawu oti "adadula phazi" akutanthauzanji?
____________________________________________(1Malikisi)

b. Kodi kuvula chipewa pamaso pa akuluakulu kumatanthauzanji?
____________________________________________(1 Malikisi)
c. Perekani ntchito imodzi ya zikwangwani za pamsewu.
____________________________________________(1 Malikisi)

5. Kupanga ziganizo

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa.

a. mtolankhani ____________________________________
b. mosamala ____________________________________
c. wokongola____________________________________
d. khu____________________________________
e. ndiponso____________________________________

**GAWO D.**

**Mafunso 6 mpaka 10 sankhani mtundu wa mawu omwe atsekedwa mnzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

6. <u>Khalidwe </u>limeneli walitenga kuti?
   A. Mfotokozi C. Mneni
   B. Dzina D. Mlumikizi

7. <u>Ogo ine!</u> Mphale ija yataika.
   A. Mvekero C. Mperekezi
   B. Mneni D. Mfuliro

8. <u>Bwanji</u> sunabwere?
   A. Mperekezi C. Muonjezi
   B. Mneni D. Mlowammalo

9. Wandibera<u> limene</u> ndagula.
   A. Mlowammalo C. Mfotokozi
   B. Mneni D. Muonjezi

10. <u>Utsadutse</u> pano palibe njira.
   A. Mfotokozi dzina C. Mperekezi
   B. Dzina D. Mneni

**Mafunso 11 mpaka 15. Sankhani kanenedwe ka aneni ka ziganizo zotsatirazi.**

11. Kodi mukulemba mayeso?
   A. Kufunsa C. Kopempha
   B. Kolamula D. Kachifuniro

12. Mutipatseko zovala zanuzo.
   A. Kofotokoza C. Kopempha
   B. Kachifundo D. Kolamula

13. Nyamuka uzipita pompano.
   A. Kopempha C. Kofotokoza
   B. Kolamula D. Kachifundo.

14. N'chiyani watengacho?

A. Kopempha C. Kolamula
B. Kofunsa D. Kofotokoza.

15. Chonde, ndimvereni chisoni.
A. Kachifuniro C. Kovomera
B. Kolamula D. Kufotokoza

**Mafunso 16 mpaka 20 sankhani ntchito za aperekezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

16. Agogo apita ku msika.
A. Kusonyeza umwini C. Kusonyeza nthawi
B. Kusonyeza malo D. Kusonyeza mbali

17. Achimwene abwera nthawi ya madzulo.
A. Kusonyeza mbali C. Kusonyeza malo
B. Kusonyeza chipangizo D. Kusonyeza ntahwi

18. Nyumbayi ndi ya aNambewe.
A. Kusonyeza m'gwirizano C. Kusonyeza nthawi
B. Kusonyeza umwini D. Kusonyeza malo

19. Yohane amumenya ndi mpini.
A. Kusonyeza nthawi C. Kusonyeza chipangizo
B. Kusonyeza nthawi D.Kusonyeza malo

20. Dzuwa limalowera ku madzulo.
A. Kusonyeza mbali C. Kusonyeza umwini
B. Kusonyeza nthawi D. Kusonyeza chipangizo.

**Mafunso 21 mpaka 25. Sankhani mvekero woyenera kukhala mu m'pata uli mchiganizo chilichonse mmusimu.**

21. Kumbuka anangoti ___________ watulukira.
A. A. Vumbu C. Balamanthu
B. Mbwe D. Fwanthu.

22. Atate ali ____________ pakhonde.
A. Mbuu C. Phe
B. Ndwi D. Khuma

23. Mbandayo idangoti ________ kusowa chonena.
A. Jenkha C. Yasa
B. Phii D. Zi

24. Anyamuka m'bandakucha kuli___________.
A. Mbuu C. Psu
B. Mbee D. Bi

25. Pasukulu panali _______ .
A. Ndwi C. Mbuu
B. Zi D. Phee

**Mafunso 26 mapaka 30. Sankhani mitundu ya nsintho wa aneni m'ziganizo zotsatirazi.**

26. Agalu alumana zedi.
A. Wochititsa C. Wobwereza bwereza
B. Wochititsitsa D. Wochitirana

27. Nkhosa yagundidwa ndi njinga.
A. Wochitidwa C. Wochitirana
B. Wochititsa D. Wochititsitsa

28. Malita wabesa ndalama zonse.
A. Wochitirana C. Wochitidwa
B. Wobwerezabwereza D. Wochititsa.

29. Iye amadutsadutsa pano.
A. Wochitirana C. Wobwerezabwereza
B. Wochititsa D. Wochititsitsa

30. Boma lapereka chimanga kwa anthu ovutika.
A. Wochitirana C. Wochititsitsa
B. Womchitira D. Wobwerezabwereza

**Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.**

31. Khoswe akakhala pa mkhate sapheka.
A. Mlandu ukakhala wako umaweluzika bwino
B. Mlandu wa m'bale umavuta kuweluza
C. Mlandu ukakhalitsa umavuta kuweluza
D. Mlandu wa mfumu umaweluzika bwino.

32. Fodya wako ndi uyo ali pamphuno wapachala ngwamphepo.
A. Kudalira zinthu zomwe zili zako
B. Kudalira zinthu zobwera
C. Kudalira zintu zopatsidwa
D. Kudalira zintu zanzako, sibwino

33. Kuwongola mtengo mpoyamba.
A. Kudulira mtengo usanakule kumapindulitsa
B. Ndi bwino kusamalira mtengo tchile lisanakule
C. Ndibwino kukonza zinthu zisanalakwikwe
D. Kukonza tsogolo ndi kwabwino kwambiri

34. Chikumbutsa nkhwangwa mchisanu.

A. Zinthu zina zimafunika panthawi yake.
B. Ntchito zina zinafunika kuthandizana.
C. Ntchito zimafunika kuzigwira utakonzeka
D. Zinthu zina zimafunika nthawi zonse.

35. Mapanga awiri avumbwitsa.
A. Kuchita zinthu zambiri kumapindulitsa
B. Kuchita zinthu mofananitsa sikupindulitsa
C. Kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi umapambana.
D. Kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi sikupindulitsa.

**Mafunso 36 mpaka 40. Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikirozamkalembedwe zoyenera m'ziganizo zotsatirazi.**

36. A. Amayi adati, "Choka iwe mwana wakuba".
B. amayi adati, "choka iwe mwana wakuba".
C. Amayi adati. Choka iwe mwana wakuba.
D. Amayi adati choka iwe mwana wakuba?

37. A. Aphunzitsi athu atenga kope pensulo ndi lula
B. aphunzitsi athu atenga kope pensulo ndi lula.
C. Aphunzitsi athu atenga kope, pensulo ndi lula.
D. Aphunzitsi athu atenga, kope, pensulo ndi lula?

38. A. Mariya amayenda monyada?
B. Mariya amayenda monyada.
C. maliya amayenda monyada!
D. maliya amayenda monyda.

39. A. Kodi Chimwemwe wanyamula zingati
B. Kodi chimwemwe, wanyamula zingati.
C. Kodi chimwemwe wanyamula zingati!
D. Kodi Chimwemwe wanyamula zingati?

40. A. Yohane M'nyunga amakonda kuyimba nyimbo.
B. yohane m'myunga amakonda kuimba nyimbo?
C. Yohane mnyunga amakonda kuimba nyimbo!
D. Yohane M'nyunga amakonda, kuimba nyimbo.

**Mafunso 41 mpaka 45. Sankhani chachikazi cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

41. Ndaona wafika ndi <u>atatavyala</u> ake.
A. Atengwa C. Amayi
B. Apongozi D. Atate.

42. Fisi wagwira <u>kachipsopsolo</u> kaja.
A. Kathazi C. Kamkota
B. Kankhunda D. Kamsoti.

43. <u>Nkhunzi</u> ya agogo yathawa m'khola.
A. Msoti C. Msona
B. Nthoni D. Mkota

44. <u>Mfumu</u> yathu ndi yankhanza.
A. Mfumakazi C. Mfumukazi
B. Ntchembere D. Mtenga

45. Talandira <u>zambwe</u> zinayi kochokera kwa a gogo.
A. Nkhunda C. Nkhosa
B. Mkota D. Mbuzi

## MAFUNSO ATHERA APA